

**KUKULA NDI MAKHALIDWE ABWINO:  
ZOWONJEZERA**

**ACHINYAMATA (KALASI YACHIWIRI)**

Wolembe **Pastor J. J. Lim**  
Ndi maganizo ena ochokera kwa **Pastor David Higgs**

Wotanthauzira ndi kukonza mu Chichewa ndi **Rev. Rex Chitekwe** komanso **Rev. Precious Kanyowa**

Losindikizidwa December 2010

## **KUKULA NDI MAKHALIDWE ABWINO**

Wolembe **Pastor J. J. Lim**  
Ndi maganizo ena ochokera kwa **Pastor David Higgs**

Wotanthauzira ndi kukonza mu Chichewa ndi **Rev. Rex Chitekwe** ndi **Rev. Precious Kanyowa**

Bukuli lasindikizidwa mu 2010 ndipo eni ake ndi a Pilgrim Covenant Church.

Chichewa version © 2012 Gratia Dei Sola Media  
Lasindikizidwa ndi Grata Dei Sola Media  
Blk 203B, Henderson Road , #07-07, Singapore 159546  
Website: [www.gdsmedia.org](http://www.gdsmedia.org)  
Email: [gdsmedia.sg@gmail.com](mailto:gdsmedia.sg@gmail.com)

Palibe akuloledwa kusindikiza kapena kuchulukitsa buku ili ngakhale za mkatimu

**Synod ya Evangelical Presbyterian Church (EPC) ku Malawi ndi ku Mozambique  
inavomereza mu chaka cha 2012 kuti bukuli lizigwiritsidwa  
ntchito mu mipingo yawo yonse.**

## ZAMKATIMU

MAU OYAMBIRIRA.....	5
PHUNZIRO 1: CHIKONDI .....	6
PHUNZIRO 2: CHIMWEMWE .....	7
PHUNZIRO 3: MTENDERE.....	8
PHUNZIRO 4: CHIKHULUPILIRO.....	9
PHUNZIRO 5: KUMVETSERA .....	10
PHUNZIRO 6: KUMVERA MULUNGU .....	11
PHUNZIRO 7: KULEMEKEZA ENA NDI KUDZIPEREKA.....	12
PHUNZIRO 8: KUDZICHEPETA .....	13
PHUNZIRO 9: KUFATSA .....	14
PHUNZIRO 10: KUNENA ZOONA .....	15
PHUNZIRO 11: KUGANIZIRA ENA.....	16
PHUNZIRO 12: KUKHALA OKHUTITSIDWA .....	17
PHUNZIRO 13: KUTHOKOZA.....	18
PHUNZIRO 14: KUKHULULUKA.....	19
PHUNZIRO 15: MKWIYO.....	20
PHUNZIRO16: KUKHULUPIRIKA NDI UDINDO .....	21
PHUNZIRO 17: KUKHULUPIRIKA .....	22
PHUNZIRO 18: CHIKHALIDWE CHABWINO NDI KUSUNGA MWAMBO.....	23
PHUNZIRO 19: KUDEKHA MTIMA DI KUPILIRA.....	24
PHUNZIRO 20: KUGWIRA NTCHITO MOLIMBIKA NDI MOSAMALA.....	25
PHUNZIRO 21: NZERU .....	26
PHUNZIRO 22: KUYERA MTIMA.....	27
PHUNZIRO 23: KUDZILETSA.....	28
PHUNZIRO 24: KUPEMPHERA.....	29
PHUNZIRO 25: KULINGALIRA MOZAMA.....	30

## MAU OYAMBIRIRA

Anthu ambiri amaganiza kuti kuloweza pamtima ngati njira yophunzitsira ndi njira ya nkhanza. Koma Mau a Mulungu amatiphunzitsa kuti sitikuyenera “kungogwiritsitsa kokha zokhazo zimene tamva” (1 Tim 1:13), komanso kuloweza pamtima mauwo, monga Davide akunenera kuti: “Ndinawabisa mau anu mumtima mwanga kuti ndisalakwire inu” (Mas119:11). Komanso, zinthu zomwe timaloweza pamtima tili aang'ono, zimakhazikika mmoyo wathu onse.

Nchifukwa chake makalasi a katekisiru mu mpingo wa PCC ndi EPC monganso mipingo yonse yokonzedwanso (Reformed Churches), amalimbikitsa kuloweza pamtima. Mwa njira ina iriyonse tikufuna kuwonetsetsa kuti ana athu akumvetsa zomwe akuloweza. Chodziwika bwino lomwe nchakuti ana amatha kuloweza asanamvetse (chimodzimodzi monga momwe amatha kuwerenga asanadziwe kumvetsa nkhani). Choncho, tiwalimbikitsa ndi kuwaphunzitsa kuloweza pamtima pamsinkhu umene angathe kutero, ngakhale tikuzindikira kuti katekisiru ndi mavesi oloweza zingakhale pamwambamwamba mumtima mwawo. Tikuchita zimenezi chifukwa Mulungu akayamba kugwira ntchito yake mmitima mwawo, (ngakhale pamene ali ana), mauwa adzakhazikika mmitima mwawo ngati mwala wa panyanja womira panso pamene dzuwa lawala ndikusungunula madzi oumawo. Kodi Ambuye sanatiphunzitse kuti ntchito ina ya Mzimu Woyera ndikukhazikitsa mumtima mwathu zomwe taphunzira? (Yoh 14:26)

Kabukuka, komwe mutu wake ndi Kukula ndi Makhalidwe Abwino, talemba okulirako kuti agwiritse ntchito ( atamaliza mabuku katekisiru woyamba aja a Mbiri ya Baibulo). Sitingaphunzitse za makhalidwe pakungoloweza kokha ayi. Koma mavesiwa adzapereka maziko abwino kwa ana athu pamene akuyesayesa kukhala ndi makhalidwe abwino kudzera mmoyo wawo komanso pogwiritsa ntchito Mau a Mulungu. Tikuvomereza kuti anawa aloweze pamtima yankho la funso (mau opezeka kumbuyo kwa mzere wautali '\_\_\_'); ndipo ngati angathe, alwezanso vesi lotsatira.

Tikupempha makolo, makamaka abambo, kuti akhale ndi nthawi yofotokozera ana awo mavesi ndi kugawana nawo zina zomwe iwo akomana nazo pa moyo wawo zomwe zingathandize anawo kumvetsa ndi kugwiritsa ntchito mavesiwo mmoyo wawo.. Kuwonjezera apo, ndikuvomerezanso kuti mavesiwo awayike chizindikiro mbaibulo mwawo kuti ngati aiwala mavesi amene aphunzirawo, athe kuwapeza mosavuta.

Pa tsiku la Mulungu, aphunzitsi akatekisiru adzigwira ntchito yophunzitsa ana anu. Aole ana kukambirana zomwe aphunzira. Abwereze mavesi omwe aloweza mmodzimodzi. Ana adzilemba (moyayang'aniridwa ndi makolo) nkhanzi ya mawu 100 pa mutu wa phunziro la sabata yotsatira ngati ntchito yowonjezera. Aphunzitsi alinso ndi ufulu wopereka ntchito zina.

Tikupempha makolo ndi aphunzitsi kuti athe kugwiritsa ntchito muyeso woyenera poyesera mwana aliyense. Pamene ana akukula mosiyana wina ndi mzake, kumakhala kovuta kwa ena kuloweza tsamba lathunthu la Mau a Mulungu. Ngati izi zili zovuta, auzeni aphunzitsi ake kuti angobwereza zokhazo zomwe anakwanitsa kuloweza. Chomodzimodzinso ana ena atha kuwona chovuta kulemba nkhanzi. Ntchito yophunzira ikhale yokoma osati yozunza. Ambuye adalitse ntchito yathu yonse, mwa Mzimu Woyera ataloweza ndi kulandira Mauwa ndi kuphatikizana ndi chikhulupiliro mmitima mwa anawa, abereke zipatso mu ulemelero wa Khristu Ambuye wathu.

Pastor J.J. Lim  
15 Nov 2002; 27 May 2005

## PHUNZIRO 1: CHIKONDI

### F1.1 Lamulo lopambana ena onse ndi liti?

Kukonda Mulungu kotheratu. \_\_\_\_”Lamulo loyambilira ndi ili: Mvera Israeli; Ambuye Mulungu wathu, Ambuye ndiye mmodzi; Ndipo uzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako onse, ndi nzeru zako zonse, ndi mphamvu yako yonse: Ili ndilo lamulo loyamba.” (Marko 12:29-30)

### F1.2 Nenani lamulo lachiwiri.

Kukonda ena monga ndidzikondera ine mwini. \_\_\_\_” Ndipo lachiwiri ndi ili: Udzikonda mzako monga udzikonda mwini, palibe lamulo lina loposa awa.” (Mar 12:29-31)

### F1.3 Lamulo latsopano ndi lotani?

Kukonda okhulupilira anzathu monga Khristu amatikondera. “Ndikukupatsani inu lamulo latsopano, kuti mukondane wina ndi mzake; monga ndakonda inu, kuti inunso mukondane wina ndi mzake. Mwa izi adzazindikira onse kuti muli akuphuzira anga, ngati muli nacho chikondano wina ndi mzake. (Yoh 13:34-35)

### F1.4 Kodi chikondi ndi ungwiro wofunika?

Inde, chifukwa popanda chikondi ndiri chabe. \_\_\_\_”Ndingakhale ndili nacho chikhulupiliro chonse, kuti ndikasendeza mapiri, koma ndiribe chikondi ndiri chabe. Ndipo ndingakhale ndipereka chuma changa chonse kudyetsa osauka, ndipo ndingakhale ndipereka thupi langa alitenthe mmoto, koma ndiribe chikondi, sindipindula kanthu ayi.” (1 Ako 13:2b-3)

### F1.5 Mukonde ndani?

Aliyense kuphatikizapo adani anga. \_\_\_\_”Koma ine ndinena kwa inu: Kondanani nao adani anu; ndikupempherera iwo akunzunza inu.” (Mat 5:44)

### F1.6 Muphuzira kwa yani kukonda anzanu?

Kwa ambuye Yesu omwe ndi chitsanzo chopambana cha chikondi. \_\_\_\_”Umo tizindikira chikondi , popezalyeyu anapereka moyo wake chifukwa cha ife; ndipo ife tiyenera kupereka moyo wathu chifukwa cha abale. “ (1Yoh 3:16)

### F1.7 Mukonde bwanji?

Muzolankhula ndi zochita zathu. \_\_\_\_”Koma iye amene ali nacho chuma cha dziko lapansi, naona mbale wake ali wosowa ndi kutsekereza chifundo chake pommana iye, nanga chikondi cha Mulungu chikhala mwa iye bwanji? Tiana tisakonde ndi mau, kapena ndi lilime, komatu ndi kuchita ndi mchoonadi.” (1 Yoh 3:17-18)

### F1.8 Kodi musakonde wina aliyense mumpingo?

Ayi, ndiyenera kukonda abale onse. \_\_\_\_”Munthu akati kuti ndikonda Mulungu, nadana naye mbale wake, ali wabodza: pakuti iye wosakonda mbale wake amene wamuona, sakhoza kukonda Mulungu amene sanamuona.” (1 Yoh 4:20)

### F1.9 Wina akakupsetsani mtima, mumkondebe?

Inde, chikondi chimakwirira machimo ambirimбири. \_\_\_\_”Koposa zonse mukhale nacho chikondano chenicheni mwa inu nokha; pakuti chikondano chikwiriritsa unyinji wa machimo.” (1 Pet 4:8)

### F1.10 Kodi izi zitanthauza kuti chikondi chili chosaona?

Ayi; \_\_\_\_”(Chikondi) sichikondwera ndi chinyengo koma chikondwera ndi choonadi.” (1 Ako 13:6 onaninso Lev 19:17)

## PHUNZIRO 2: CHIMWEMWE

### F2.1 Ali wa chimwemwe ndi ndani?

Mkristu aliyense akuyenera kukhala wachimwemwe. \_\_\_\_”Sekererani mwa Yehova, ndipo kondwerani inu wolungama mtima; Ndipo fuulani mokondwera nonsenu oongoka mtima.” (Mas 32:11)

### F2.2 Tisangalale nthawi iti?

Nthawi zonse. \_\_\_\_”Kondwerani mwa Ambuye nthawi zonse; ndibwerezanso kutero, kondwerani.” (Afi 4:4)

### F2.3 Chimwemwe chenicheni tingachipeze kuti?

Mwa Mulungu. \_\_\_\_”Mudzandidziwitsa njira ya moyo: pankhope panu pali chimwemwe chokwanira, mdzanja lanu la manja muli zokondweretsa zomka muyaya.” ( Mas 16:11)

### F2.4 Musangalale chifukwa chiyani?

Ndiyenera kukondwera chifukwa ndiwadziwa Ambuye amene amandipulumutsa. \_\_\_\_”Ndidzakondwa kwambiri mwa Yehova, moyo wanga udzakondwera mwa Mulungu wanga:pakuti Iye wandiveka ine ndi zovala za chipulumutso, nandifunda chofunda cha chilungamo, monga mkwati avala nduwira, ndi monga mkwatibwi adzikometsa yekha ndi miyala ya mtengo.” (Yes 61:10; onaninso Aro 5:11)

### F2.5 Ndikhale wotani pamene ndikukondwa?

Ndikhale wofatsa ndi wodzichepetsa. \_\_\_\_”Ofatsanso kukondwa kwawo kudzachuluka mwa Yehova, ndi a umphawi a mwa anthu adzakondwera mwa Woyera wa Israeli.” (Yes 29:19)

### F2.6 Ngati mukudutsa nthawi yovuta, kodi mukuyeneranso kukondwera?

Inde, chifukwa Mulungu akugwira ntchito yake ya chaulere mwa ine. \_\_\_\_”Muchiyese chimwemwe chokha, abale anga, mmene mukugwa mmayesero a mitundumitundu; Pozindikira kuti chiyesedwe cha chikhulupiliro chanu chichita chipiliro.” (Yak 1:2-4; onaninso 1 Pet 1:6)

### F2.7 Ngati anzathu akusangalala ndi za mdziko la pansi pano, kodi nanunso musangalale nawo?

Ayi, ngati akuchita zoipira Mulungu. \_\_\_\_”Kondwera ndi unyamata wako, mnyamata iwe; mtima wako nukasangalale masiku a unyamata wako, nuyende mnjira za mtima wako, ndi monga maso ako aona; koma dziwitsa kuti adzanena nawe mlandu wa zonsezi.” (Mla 11:9)

### F2.8 Kodi kunena nthabwala ndi kumaseka za nthabwalazo ndi kusangalala?

Palibe cholakwa china chilichonse kuseka nthabwala zabwino, koma chimwemwe chenicheni chimapezeka pamene tikhala othokoza Mulungu pazonse. \_\_\_\_”Pakuti kuseka kwa chitsiru kunga minga iri kuthetheka pansi pa mphika; ichinso ndi chabe.” (Mla 7:6)

### F2.9 Mungakondwere pamene mukusewera?

Inde, ndiyenera kuthokoza Mulungu chifukwa cha zinthu zabwino zosangalatsa. \_\_\_\_”Mtima wosekerera uchiritsidwa bwino; koma mtima wosweka uphwetsa mafupa.” (Miy 17:22)

### F1.10 Mungakondwe bwanji pamene simukusewera?

“Pochita zonse popanda madandaulo ndi makani”. (Afi 2:14)

## PHUNZIRO 3: MTENDERE

### F3.1 Kodi Mulungu amafuna kuti tikhale a mtendere?

Inde, chifukwa lye ndi Mulungu wa mtendere, choncho amafuna kuti ifenso tikhale a mtendere. \_\_\_ "Chifukwa chake tilondole zinthu za mtendere, ndi zinthu za kulimbikitsana wina ndi mnzake."  
(Aro 14:19)

### F3.2 Kukhala wa mtendere zitanthauza kutani?

Ndikukana kukangana ndi wina aliyense. \_\_\_ "Koma nzeru yochokera kumwamba iyamba kukhala yoyera, nikhalanso yamtendere, yaulere, yomvera bwino, yodzala chifundo ndi zipatso zabwino, yopanda tsankhu, yosadzikometsera pamaso. Ndipo chipatso cha chilungamo chifisedwa mumtendere kwa iwo akuchita mtendere." (Yak 3:17-18)

### F3.3 Mungakhale bwanji pamtendere pamene ena ali olongolola?

Ndisade nkhwana ndi ena bola ngati ine ndili wa mtendere. \_\_\_ "Ngati nkutheka, monga momwe mukhoza, khalani ndi mtendere ndi anthu onse." (Aro 12:18)

### F3.4 Ngati anzanu akangana ndi ena, inu mutani?

Ndiyese yese kudzetsa mtendere pakati pawo. \_\_\_ "Odala ali akuchita mtendere; chifukwa adzatchedwa ana a Mulungu." (Mat 5:9)

### F3.5 Mungakhale bwanji mwamtendere ndi awo amene simugwirizana nawo?

Pokhala wodzichepetsa ndi wofatsa. \_\_\_ "Ndi kuwonetsera kudzichepetsa konse, ndi chifatso, ndi kuonetsera chipiliro, ndi kulolerana wina ndi mnzake, mwa chikondi; ndi kusamalitsa kusunga umodzi wa Mzimu mwa chimangiriro cha mtendere." (Aef 4:2-3; onaninso 2 Tim 2:24-25)

### F3.6 Kodi nkofunika kuti mukhale a mtendere kunyumba kwanu?

Inde; pakhomo pa mkhristu payenera phakhale pa mtendere. \_\_\_ "Nyenyiswa youma, pokhala mtendere, iposa nyumba yodzala nyama ya nsembe, pali makangano." (Miy 17:1)

### F3.7 Mtendere mu mpingo ngofunika?

Inde; Mulungu amasangalala pamene mumpingo muli mgwirizano ndi mtendere. \_\_\_ "Onani, nokokoma ndi kokondweretsa ndithu kuti abale akhale pamodzi!" (Mas 133:1)

### F3.8 Mungalimbikitse bwanji mtendere mumpingo?

Pokana kukangana ndi ena komanso kupempherera mtendere. \_\_\_ "Futuka pa zoipa, nuchite zabwino, funa mtendere ndi kuulondola." (Mas 34:14); "Mupempherere mtendere wa Yerusalemu; akukonda inu adzaona phindu." (Mas 122:6)



## PHUNZIRO 4: CHIKHULUPILIRO

### F4.1 Chikhulupiliro ndi chiyani?

Chikhulupiliro ndi kumvera. \_\_\_\_”Koma chikhulupiliro ndicho chikhazikitso cha zinthu zoyembekezeka, chiyesero cha zinthu zosapenyeka.” (Ahe 11:1)

### F4.2 Kodi chikhulupiliro ndi chofunika?

Inde; popanda chikhulupiliro sitingakondweretse Mulungu. \_\_\_\_”Koma wopanda chikhulupiliro sikutheka kunkondweretsa; pakuti iye wakudza kwa Mulungu ayenera kukhulupilira kuti alipo, ndi kuti ali wobwezera mphotho iwo akumfuna Iye. (Ahe 11:6)

### F4.3 Kodi chikhulupiliro ndi chachilengedwe mwa anthu onse?

Ayi; munthu pachilengedwe pake alibe chikhulupiliro. \_\_\_\_”Ndipo inu anakupatsani moyo, pokhala munali akufa ndi zolakwa, ndi zochimwa zanu, ... Pakuti muli opulumutsidwa ndi chisomo cha kuchita mwa chikhulupiliro, ndipo ichi chosachokera kwa inu: chiri mphatso ya Mulungu. (Aef 2:1, 8)

### F4.4 Mulungu amapereka chikhulupiliro kwa ndani?

Kwa osankhidwa ake. \_\_\_\_”Ndipo anakhulupilira onse amene anaikidwiratu ku moyo wosatha.” (Mac 13:48b)

### F4.5 Chikhulupiliro ndiko kumvera, kodi timvere chiyani?

Timvere Ambuye Yesu Khristu kuti tikapulumeke. \_\_\_\_”Koma podziwa kuti munthu sayesedwa wolungama pa ntchito ya lamulo, koma mwa chikhulupiliro cha Yesu Khristu, ifedi tinakhulupira kwa Yesu Khristu, kuti tikayesedwe olungama ndi chikhulupiliro cha Khristu, ndipo si ndi ntchito za lamulo ; pakuti palibe munthu adzayesedwa i wolungama ndi ntchito za lamulo.” (Aga 2:16)

### F4.6 Mungakule bwanji mchikhulupiliro?

Pomva Mau a Mulungu. \_\_\_\_Chomwecho chikhulupiliro chidza ndi mbiri, ndi mbiri idza mwa mau a Khristu.” (Aro 10:17)”Ambuye ndikhulupilira; thandizani kusakhulupilira kwanga.” (Marko 9:24b)

### F4.7 Kodi alipo okhulupilira onama kapena amene amanamizira kukhulupilira?

Inde, alipo ambiri padziko lapansi pano. \_\_\_\_”Ndipo za pa thanthwe ndiwo amene, pakumva, alandira mau ndi kukondwera; koma alibe mizu; akhulupilira kanthawi, ndipo pa nthawi yamayesedwe angopatuka.” (Luk 8:13; onaninso Mat 13:20-21; Mac 8:13, 20-23; Mac 26:27-28)

### F4.8 Kodi chikhulupiliro nchofunika popemphera?

Inde, pakuti Mulungu sayankha mapemphero a anthu osakhulupilira. \_\_\_\_”Ndipo zinthu irizonse mukazifunsa nkuzipemphera ndi kukhulupilira, mudzalandira.” (Mat 21: 22)

### F4.9 Kodi chikhulupiliro nchofunika pa moyo wa chikhristu?

Inde, chifukwa popanda chikhulupiliro tingamezedwe ndi za mdziko lapansi. \_\_\_\_”Ndipo ichi ndi chilako tililaka nacho dziko la pansu, ndicho chikhulupiliro chathu. Koma ndani iye wolilaka dziko la pansu koma iye amene akhulupilira kuti Yesu ndiye Mwana wa Mulungu?” (1 Yoh 5:4b-5)

## PHUNZIRO 5: KUMVETSERA

### F5.1 Kodi mulungu akutilamula kukhala omvetsera ( mmakutu, mmaso ndi mumtima)?

Inde, Solomoni akuphunzitsa kukhala omvetsera. \_\_\_\_”Mwananga, tamvera mau anga; cherera makutu ku zonena zanga. Asachoke ku maso ako; Uwasunge mkati mwa mtima wako.” (Miy 4:20-21)

### F5.2 Tiphunzira kumvetsera kuchokera kwa yani?

Kwa Ambuye Yesu amene anali chitsanzo chopambana cha kumvetsera. \_\_\_\_”Ndipo pakupita masiku atatu, anampeza lye mkachisi, anali kukhala pakati pa aphunzitsi, namva iwo , nawafunsanso mafunso.” (Luk 2:46).

### F5.3 Timvetserere makamaka kwa ndani?

Kwa Ambuye Yesu Khristu. \_\_\_\_”Nkhosa zanga zimva mau anga, ndipo lne ndizizindikira, ndipo zinditsata ine.” (Yoh 10:27; onaninso vesi 3-4)

### F5.4 Mungamvetserere bwanji kwa Ambuye?

Pomvetsera ndi kulandira mokondwera Mau a Mulungu. \_\_\_\_”amenewa (a Bereya) anali mfulu koposa a m’Tesalonika, popeza analandira mau ndi kufunitsa kwa mtima wonse, nasanthula m’malembo , masiku onse, ngati zinthu zotero.” (Mac 17:11; onaninso I Atesa 2:13)

### F5.5 Kodi nkofunika kumvetsera pamene Mau a Mulungu akulalikidwa?

Inde, popeza “Chikhulupiliro chidza ndi mbiri, ndi mbiri idza mwa mau a Khristu.” (Aro 10:17)

### F5.6 Nanga ngati mukudziwa kale zomwe zikulalikidwa kapena kuphunzitsidwa?

Ndiyenera kumvetserabe kuti ndiphunzire zina zatsopano kapena ndikumbutsidwe zina. \_\_\_\_ “Chifukwa chake iye wakuyesa kuti ali chiliri, ayang’anire kuti angagwe.” (1 Ako 10:12)

### F5.7 Kodi mukhulupilire chilichonse chimene mwamva?

Ayi, ndingokhulupilira zokhazo zomwe zikugwirizana ndi Baibulo. \_\_\_\_”Yesani zonse, sungani chokomacho.” (1 Ate 5:21)

### F5.8 Chimachitika nchiyani ngati mwalephera kumvetsera?

Sindingalandire madalitso kuchokera kwa Mulungu. \_\_\_\_”Nchifukwa chake yang’anirani mamvedwe anu; pakuti kudzapatsidwa kwa iye amene ali nacho; ndipo kwa iye amene alibe, chidzachotsedwa, chingakhale chija aoneka ngati ali nacho.” (Luk 8:18)

### F5.9 Ndingaphunzire bwanji kumvetsera ena?

Polankhula modekha ndi kutchera khutu pomvetsera. \_\_\_\_”Mudziwa abale anga okondeka, kuti munthu aliyense akhale wotchera khutu, wodekha polankhula, wodekha pakupsa mtima.” (Yak 1:19)

## PHUNZIRO 6: KUMVERA MULUNGU

### F6.1 Kodi Baibulo litilamula kumvera Mulungu?

Inde; Baibulo likutilamula pena paliponse kumvera Mulungu. \_\_\_Mwachitsanzo: “Mudziyenda kutsata Yehova Mulungu wanu, ndi kumuopa, ndi kusunga malamulo ake, ndi kumtumikira lye, ndi kummamatira.” (Deu 13:4; onaninso Mla 12:13)

### F6.2 Kodi akhristu akuyenera kumvera Mulungu koposa wina aliyense pansu pano?

Inde; monga ana ake a Mulungu tiyenera kumumvera. \_\_\_”Ndipo tsopano, ngati mudzamvera mau anga ndithu ndi kusunga chipangano changa, ndidzakuyesani chuma changa chapadera koposa mitundu yonse ya anthu; pakuti dziko lonse lapansi ndi langa.” (Eks 19:5; onaninso Deu 7:9)

### F6.3 Chifukwa chiyani makamaka akhristu akuyenera kumvera Mulungu?

Akhristu akuyenera kumvera Mulungu mothokoza ndi mwachikondi chifukwa adatipulumutsa mwa Khristu. \_\_\_”Koma inu ndinu mbadwa yosankhika, ansembe yachifumu, mtundu woyera mtima, anthu amwini wake, kotero kuti mukalalikire zoposazo za lye amene anakuitanani muturuke mumdima, mulowe kuunika kwake kodabwitsa. Inu amene kale simunali anthu, koma tsopano muli anthu a Mulungu; amene kale simunalandira chifundo, koma tsopano mwalandira chifundo.” ( 1 Pet 2:9-10; onaninso v 5; 1 Ako 6:19-20; Aro 6:13; ndi 12:1-2)

### F6.4 Tiphunzira kumvera kuchokera kwa yani?

Kuchokera kwa Ambuye Yesu Khristu. \_\_\_”Angakhale anali Mwana, anaphunzira kumvera ndi izi adamva kuwawa nazo.” (Ahe 5:8)

### F6.5 Kodi kumvera nkofunika?

Inde; kuposa miyambo yonse ya chipembedzo. \_\_\_”Ndipo Samuel anati, Kodi Yehova akondwera ndi nsembe zopsereza ndi nsembe zophera, monga ndi kumvera mau a Yehova? Tawonani, kumvera ndiko kokoma koposa nsembe, kutchera khutu koposa mafuta ankhosa zamphongo.” (1 Sam 15:22)

### F6.6 Ngati munthu samvera lamuloli chimachitika nchiyani?

Mapemphero anga sadzamveka kwa Mulungu. \_\_\_”Woperewetsa khutu lake kuti asamve chilamulo, ngakhale pemphero lake linyansa.” (Miy 28:9)

### F6.7 Nzotheke kusankha kumvera malamulo ena ndi kukana ena?

Ayi; Ndiyenera kumvera malamulo onse mokondwa ndi chithandizo cha Mulungu. \_\_\_”Potero muzisamalira kuchita monga Yehova Mulungu wanu anakulamulirani; musamapatuka ku lamanzere kapena kulamanja.” (Deu 5:32)

### F6.8 Mungatani ngati mukufuna kukhala omvera Mulungu koposa?

Ndipempherere chaulere cha Mulungu. Ndipemphere monga mulembi wa Masalimo . \_\_\_”Mundizindikiritse, ndipo ndidzasunga malamulo anu; ndidzawasamalira ndi mtima wanga onse.” (Mas 119:34; onaninso 143:10)

### F6.9 Mungakhale ndi chikhulupiliro popanda kumvera?

Ayi; chikhulupiliro chopanda kumvera nchakufa. \_\_\_”Khalani akuchita mau, osati akumva okha, ndi kudziyenga nokha.” (Yak 1:22; onaninso vesi 25)

### F6.10 Mungakonde Mulungu koma osamumvera?

Ayi; kukonda Mulungu ndikusunganso malamulo ake. \_\_\_”Pakuti ichi ndi chikondi cha Mulungu, kuti tisunge malamulo ake: ndipo malamulo ake sali olemetsa.” (1 Yoh 5:3, onaninso Yoh 14:15)

## PHUNZIRO 7: KULEMEKEZA ENA NDI KUDZIPEREKA

### F7.1 Kodi Baibulo limatilamula kulemekeza audindo?

Inde; lamuloli laperekedwa mlamulo lachisanu. \_\_\_\_”Ananu mverani akukubalani mwa Ambuye, pakuti ichi nchabwino. Lemekeza atate ako ndi amako, (ndilo lamulo loyamba lokhala nalo lonjezano)” (Aef 6:1-2; onaninso Eks 20:12)

### F7.2 Tiphunzira kwa ndani kulemekeza ena?

Kuchokera kwa Ambuye Yesu Khristu. \_\_\_\_”Ndipo anatsika (Ambuye Yesu) nawo pamodzi (makolo ake) nadza ku Nazareti; nawamvera iwo.” (Luk 2:51a)

### F7.3 Makolo anu muwamvere mu ziti?

Mu zonse. \_\_\_\_”Ana inu, mverani akubala inu mzonse, pakuti ichi Ambuye akondwera nacho.” (Akolose 3:20; onaninso Miy 1:8)

### F7.4 Baibulo likuti chiyani zochitira mwano makolo?

Mulungu amadana nazo. \_\_\_\_”Diso lochitira atate wache chiphwete, ndi kunyoza kumvera amake, makungubwi akumtsinje adzalikolowola, ana a mphungu adzalidya.” (Miy 30:17)

### F7.5 Kodi mukuyenera kulemekeza atsogoleri ndi abusa a mpingo?

Inde, Baibulo litiphunzitsa kuwamvera ndi kuwalemekeza. \_\_\_\_”Mverani atsogoleri anu, nimuwagonjere; pakuti alindira moyo wanu, monga akuwerengera; kuti akachite ndi chimwemwe, osati mwachisoni: pakuti ichi sichikupindulitsani inu.” (Ahe 13:17)

### F7.6 Kodi mulemekezenso atsogoleri aboma?

Inde; pakuti ngakhale osakhulupilira anawasankha ndi Mulungu. \_\_\_\_”Anthu onse amvere maulamuliro a akulu; pakuti palibe ulamuliro wina koma wochokera kwa Mulungu; ndipo amene alipo aikidwa ndi Mulungu.” (Aro 13:1)

### F7.7 Kodi mumvere olamula amene angakuchimwitseni?

Ayi; ndisamvere lamulo lililonse lomwe ndi lochimwitsa. \_\_\_\_”Ndipo anayankha Petro ndi Atumwi, nati, Tiyenera kumvera Mulungu koposa anthu.” (Mac 5:29)

### F7.8 Muchite nawo bwanji omwe ndi aakulu oposa inu kumpingo?

Ndiyenera kuwapatsa ulemu. \_\_\_\_” Mkulu usamdudzule , komatu umdandaulire ngati atate; anyamata ngati abale; akazi aakulu ngati amai; akazi aang’ono ngati alongo, mkuyera mtima konse.” (1 Tim 5:1-2)

### F7.9 Akulu tiwalemekeze bwanji?

Ndidzuke ndikuwapatsa moni pamene akubwera kwa ine. \_\_\_\_” Pali aimvi uziwagwadira, nuchitire ulemu munthu wokalamba; nuope Mulungu wako; Ine ndine Yehova.” (Lev 19:32)

### F7.10 Kodi mudzipereke kwa anzanu kumpingo?

Inde; mwa chifuniro chake cha Mulungu kwa ine. \_\_\_\_”Ndikumverana wina ndi mnzake mkuopa Khristu. (Aef 5:21)

## PHUNZIRO 8: KUDZICHEPETA

### F8.1. Chifukwa chiyani muyenera kukhala odzichepetsa?

Baibulo litilamula kukhala odzichepetsa popeza Mulungu amadana ndi kunyada. \_\_\_”Momwemonso, anyamata inu, mverani akulu. Koma nonsenu muvale kudzichepetsa kuti mutumikirane; pakuti Mulungu akaniza odzikuza, koma apatsa chisomo kwa odzichepetsa.” (1 Pet 5:5, onaninso Yak 4:6)

### F8.2. Kudzichepetsa ndiko kutani?

Kudzichepetsa sikukhala wamng'ono koma kuona zokhazo zomwe zili zotamandika mwa ena. \_\_\_”Musachite kanthu monga mwa chotetana, kapena monga mwa ulemelero wopanda pake, komatu ndi kudzichepetsa mtima, yense ayese mzake omposa iye mwini.” (Afi 2:3)

### F8.3 Mungaphunzire kudzichepetsa kuchokera kwa yani?

Makamaka kuchokera kwa Ambuye Yesu Khristu. \_\_\_Mukhale nawo mtima mkati mwanu umene unalinso mwa Khristu Yesu, ameneyo, pokhala nawo maonekedwe a Mulungu, sanachiyesa cholanda kukhala wofana ndi Mulungu, koma anadzikhuthula yekha, natenga maonekedwe a kapolo, nakhala mmfanizidwe a anthu; ndipo popezedwa mmaonekedwe ngati munthu, anadzichepetsa yekha nakhala womvera kufikira imfa, ndiyo imfa ya pamtanda.” (Afi 2:5-8)

### F8.4 Mudzichepetse bwanji?

Ndiwone ena kukhala wofunikira kuposa ine. \_\_\_”Mchikondano cha anzanu wina ndi mzake mukondane ndi chikondi chenecheni; mutsogolerane ndi kuchitira wina mzake ulemu.” (Aro 12:10)

### F8.5 Kodi kunyada ndi tchimo?

Inde; popeza Mulungu amadana ndi kunyada. \_\_\_”Maso akunyada, ndi mtima wodzikuza, ndi nyali ya oipa, ziri tchimo” (Miy 21:4)

### F8.6 Anthu amati, “Popanda kunyada sitingapambane pa china chirichonse.” Baibulo likuti chiyani pa mau amenewa?

Baibulo limati: “Kudzikuza kwa munthu kudzamchepetsa; koma wokhala ndi mtima wodzichepetsa adzalemekezedwa.” (Miy 29:23)

### F8.7 Kodi munthu wodzichepetsa angachite bwino mdera lake?

Inde; popeza ndi lonjezo la Mulungu. \_\_\_”Mphotho ya chifatso ndi kuopa Yehova ndiye chuma, ndi ulemu ndi moyo. (Miyambo 22:4 onaninso Miyambo 15:33)

### F8.8 Kodi nkulakwa kudzitama pamene mwachita bwino pa china chirichonse?

Ngati ndidzitamandira mmalo molemekeza Mulungu, Mulunguyo adzanditsitsa chifukwa cha zabwino zangazo. \_\_\_”Ndipo amene aliyense akadzikuza yekha adzachepetsedwa; koma amene adzichepetsa mwini yekha adzakulitsidwa. (Mat 23:12)

## PHUNZIRO 9: KUFATSA

### F9.1 Kodi kufatsa ndi ungiro wa chikristu?

Inde, kufatsa ndi chizindikiro cha chaulere kwa onse wokhulupilira. \_\_\_”Popeza Yehova akondwera nao anthu ake; adzakometsa ofatsa ndi chipulumutso. (Mas 149:4). Odala ali akufatsa; chifukwa adzalandira dziko lapansi.” (Mat 5:5)

### F9.2 Kupatula Ambuye Yesu, munthu wina wofatsa kwambiri amene anakhala panso ndani?

Mose ndi amene anali wofatsa kwambiri mmasiku ake. \_\_\_”koma munthuyu Mose ndiye wofatsa woposa anthu wonse a pa dziko lapansi.” (Num 12:3); koma munthu wofatsitsitsa amene anakhala pa dziko la panso ndi Ambuye Yesu amene akunena kuti “Idzani kuno kwa Ine nonsenu akulema ndi akuthodwa, ndipo ine ndidzakupulumutsani inu. Senzani goli langa, ndipo phunzirani kwa Ine; chifukwa ndiri wofatsa ndi wodzichepetsa mtima: ndipo mudzapeza mpumulo wa miyoyo yanu.” (Mat 11:28-29)

### F9.3 Kufatsa ndi kudzichepetsa kusiyana bwanji?

Kufatsa ndi kukhala wodzichepetsa ndi wodekha makamaka pamene tawopsezidwa. \_\_\_”Ambuye Yesu anaonetsa kufatsa kwawo pamene anachitidwa chipongwe sanabwezera chipongwe, pakumva zowawa sanaopsa, koma anapereka mulandu kwa Iye woweruza wolungama” (1 Pet 2:23)

### F9.4 Kufatsa nkofunika bwanji mumpingo?

Popanda kufatsa sitikhala akhristu, ndipo sipakhala umodzi mumpingo. \_\_\_” Mtumwi Paulo akunena kuti; Ndikukudandaulirani inu tsono, ine wamndende wa Ambuye, muyende koyenera mayitanidwe amene munaitanidwa nawo, ndi kuonetsera kudzichepetsa konse, ndi chifatso ndi kuonetsera chipiriro ndi kulolerana wina ndi mzake, mwa chikondi; ndi kusamalitsa kusungu umodzi wa Mzimu mwa chimangiriro cha mtendere.” (Aef 4:1-3)

### F9.5 Kodi munthu angaphunzire kukhala wofatsa?

Inde, nkofunika zedi kutero. \_\_\_”funani Yehova, ofatsa inu nonse a mdziko amene munachita chiweruzo chake; funani chilungamo, funani chifatso; kapena mudzabisika tsiku la mkwiyo wa Yehova.” (Zef 2:3)

### F9.6 Ndingaphunzire bwanji kukhala wofatsa?

Pokumbukira nthawi zonse “kufatsa ndi kudzichepetsa komwe Khristu anali nako.” (2 Ako 10:1) komanso posamiriza ena kutsatira maganizo athu. \_\_\_”ndipo kapolo wa Ambuye sayenera kuchita ndewu, komatu akhale woyenera, waulere pa zonse, wodziwakuphunzitsa, woleza, wolangiza iwo akutsutsana mofatsa; ngati kapena Mulungu awapatse iwo chitembenuziro, kukazindikira choonadi.” (2 Tim 2:24-25 komanso Tito 3:2)

### F9.7 Kodi anthu ofatsa amapindulanji ndi moyo uno?

Ambuye adzawatsogolera pa zonse zomwe adzachita. \_\_\_”Adzawatsogolera ofatsa mchiweruzo; ndipo adzaphunzitsa ofatsa njira yake.” (Mas 25:9)

## PHUNZIRO 10: KUNENA ZOONA

### F10.1 Kodi mungaphunzire kukhala woona kuchokera kwa yani?

Kuchokera kwa Ambuye Yesu Khristu. \_\_\_\_”Pakuti kudzachitika ichi mwaitanidwa; pakutinso Khristu anamva zowawa mmalo mwanu nakusiirani chitsanzo kuti mukalondole mapazi ake; amene sanachita tchimo, ndipo mkamwa mwake sichinapezedwa chinyengo.” (1 Pet 2:21-22)

### F10.2 Kodi kunena zoona polankhula nkofunika?

Inde; Mulungu amadana ndi bodza. \_\_\_\_”Milomo yonama inyansa Yehova; koma ochita mtheredi amsekeretsa.” (Miy 12:22; onaninso Aef 4:25)

### F10.3 Kodi kuchita katangale ndi chimodzimidzi kunena zonama?

Inde; katangale ndiwoletsedwa ndi mau a Mulungu. \_\_\_\_”Muyeso wonyenga unyansa Yehova; koma mulingo wamphumphu umsekeretsa.” (Miy 11:1)

### F10.4 Kodi ndi bwino kunyengezera kugwira ntchito mokhulupirika pamene bambo kapena aphunzitsi anu akuwona?

Ayi; sindiyenera kugwira ntchito mwa chinyengo. Ndiyenera kuwopa Mulungu. \_\_\_\_”Akapolo inu; mverani mzonse iwo amene ali ambuye monga mwa thupi, osati ukapolo wa pa maso monga wokondweretsa anthu, komatu ndi mtima wakulinga kumodzi, akuopa Ambuye. “(Akol 3:22)

### F10.5 Kodi ndi bwino kunena mosinjirira?

Ayi; Mulungu amadana ndi lirime losinjirira. \_\_\_\_”Yehova adzadula milomo yonse yotyasika , lirime lakudzitandira.” (Mas 12:3)

### F10.6 Kodi ndi kofunika kukonza ngati ndanena zonama?

Inde; Ngati ndanena zonama, ndiyenera kukonza ponena zoona. \_\_\_\_”Mmenemonso ndidziyesetsa ndekha ndikhale nacho nthawi zonse chikumbumtima chosanditsutsa cha kwa Mulungu ndi kwa anthu.” (Mac 24:16; onaninso 2 Ako 8:21)

### F10.7 Kodi kukhulupirika ndi ndondomeko yabwino ya moyo wathu?

Inde; \_\_\_\_”Kuongoka mtima kwa olungama kuwatsogolera; koma kukhota kwa achiwembu kudzawaononga.” (Miy 11:3; onaninso Miy 19:1)

### F10.8 Kodi kulandira ziphuphu kuti zathu zitiyendere nkoyipa?

Inde, anthu a padziko la pansi pano amalandira ziphuphu , koma akhrisu ayenera kukana kwathunthu njira zosalungama zimenezi. \_\_\_\_”Musamapotoza chiweruzo, musamasamalira munthu, kapena kulandira chokometsera mlandu; popeza chokometsera mlandu chidetsa maso a anzeru nichipitsa mau a olungama.” (Deut 16:19)

## PHUNZIRO 11: KUGANIZIRA ENA

### F11.1 Kodi Baibulo litilamula kuganizira ena?

Inde. \_\_\_\_”Munthu yense asapenyereke zake za iye yekha, koma yense apenyerekenso za mnzake.” (Afi 2:4; onaninso 1 Ako 10:24)

### F11.2 Ndani adapereka chitsanzo chachikulu cha kuganizira ena?

Ambuye Yesu Khristu. \_\_\_\_”Pakuti mudziwa chisomo cha Ambuye wathu Yesu Khristu kuti, chifukwa cha inu anakhala wosauka, angakhale anali wolemera, kuti inu ndi kusauka kwake mukakhale olemera.” (2 Ako 8:9)

### F11.3 Kuganizira ena ndiko kutani?

Ndikukhala a chifundo kwa iwo. \_\_\_\_”Ndipo ife amene tiri olimba tiyenera kunyamula zofooka za opanda mphamvu, ndi kusadzikondweretsa tokha. Yense wa ife akondweretsa mzake kumchitira zabwino zakumlimbikitsa. Pakuti Khristunso sanadzikondweretsa yekha.” (Aro 15:1-3a)

### F11.4 Kodi kuganizira ena zitanthauza kuti tisapute ena?

Ayi, kuganizira ena nthawi zina kumasowa kukonza zolakwa za ena. \_\_\_\_”Ndipo tiganizirane wina ndi mzake kuti tifulumizane ku chikondano ndi ntchito zabwino.” (Ahe 10:24; onaninso Aro 14:19)

### F11.5 kodi ulemu ndi khalidwe la ungwiro?

Inde, ulemu ndi khalidwe la kuganizira ena. \_\_\_\_”Chotsalira, khalani nonse a mtima umodzi, ochitirana chifundo, okondana ndi abale, achisomo, odzichepetsa.” (1 Pet 3:8)

### F11.6 Kodi tikuyenera kuthandiza ena?

Inde, Khristu Ambuye athu amatiphunzitsa kutumikira ena. \_\_\_\_”Nchifukwa chake, ngati ine, Ambuye ndi Mphunzitsi, ndasambitsa mapazi anu, inunso muyenera kusambitsana mapazi wina ndi mzake.” (Yoh 13:14)

### F11.7 Kuthandiza ena ndiko kutani?

Ndiko kumva nawo zowawa za ena. \_\_\_\_”Nyamuliranani zothodwetsa, ndipo kotero mufitse chilamulo cha Khristu.” (Aga 6:2)

### F11.8 Perekani zitsanzo zingapo za kuthandizana wina ndi mzake.

Kuthandiza osowa ndi kulandira alendo. \_\_\_\_”Patsani zosowa oyera mtima; cherezani aulendo. (Aro 12:13)

### F11.9 Kodi tithandizenso amene satiyamikira?

Inde, popeza Ambuye atiphunzitsa kuti, “kupatsa kutidalitsa kuposa kulandira.” (Mac 20:35)



## PHUNZIRO 12: KUKHALA OKHUTITSIDWA

### F12.1 Kodi Baibulo litilamula kukhala okhutitsidwa?

Inde, Baibulo litilamula kutero mulamulo la Mulungu la chikhumi. \_\_\_"Usasilire nyumba yake ya mzako, usasilire mkazi wake wa mzako, kapena wantchito wake wamwamuna kapena wantchito wake wamkazi, kapena ng'ombe yake, kapena buru wake kapena kanthu kalikonse kamzako." (Eks 20:17)

### F12.2 Kukhala okhutitsidwa ndi ungwiro wa chikhristu?

Inde, popeza "chipembedzo pamodzi ndikudekha chipindulitsa kwakukuru." (1Tim 6:6; komanso vesi 7 mpaka 10)

### F12.3 Ndi zotheka kukhala osauka komanso okhutitsidwa?

Kwambiri ndithu!\_\_\_"Sikuti ndinena monga mwa chiperewero, pakuti ndaphunzira ine kuti zindikwanire ziri zonse ndiri nazo. Ndadziwa ngakhale kupeputsidwa, ndadziwanso kusefukira; konseko ndi mzinthu zonse ndalowa mwambo wa kukhuta, ndiponso wakumva njala." (Afi 4:11-12)

### F12.4 Tingaphunzire kuchokera kwa yani kukhala okhutitsidwa ngakhale pamene tiri osauka?

Kuchokera kwa Ambuye Yesu Khristu Mwana wa Mulungu. \_\_\_Iye akuti, "Ankhandwe ali nazo nkhwimba zawo, ndi mbalame za mulengelenge zisa zawo, koma Mwana wa Munthu alibe potsamira mutu wake." (Mat 8:20)

### F12.5 Kodi nkwabwino kukhala osauka kulekana ndi kukhala olemera?

Ayi, sichoncho. \_\_\_ Mfumu Aguri anapemphera: "Mundichotsere kutali zachabe ndi mabodza; musandipatse umphawi ngakhale chuma, mundidyetse zakudya zondiyenera; Ndingakhute ndi kukukanani, ndi kuti, Yehova ndani? Kapena ndingasauke ndi kuba, ndi kutchula dzina la Mulungu wanga pachabe." (Miy 30:8-9)

### F12.6 Kodi kukhutitsidwa kumangokamba za kusauka kapena kulemera kokha?

Ayi, kukukhudzanso zinthu zimene zimapangitsa kuti zina zichitike komanso chikhalidwe chatu chabwino. \_\_\_"Yense mmene anaitanidwamo, abale, akhale momwemo ndi Mulungu." (1 Ako 7:24) ; komanso "Tisakhale odzikuzi, outsana, akuchitirana njiru." (Aga 5:26)

### F12.7 Tingalimbikitsidwe bwanji kukhala okhutitsidwa?

Pokumbukira lonjezo la Ambuye loti adzakhala nafe nthawi zonse. \_\_\_"Mtima wanu ukhale wosakonda chuma; zimene muli nazo zikukwanireni; pakuti iye anati, sindidzakusiya konse kungakhale kukutaya, sindidzakutaya." (Ahe 13:5)

## PHUNZIRO 13: KUTHOKOZA

### F13.1 Kodi Baibulo litilamula kuthokoza?

Inde, malo ambiri m'Baibulo litilamula kutero. \_\_\_mwachitsanzo, Mtumwi Paulo akuti: "M'zonse, yamikani; pakuti ichi ndi chifuniro cha Mulungu cha kwa inu mwa Khristu Yesu." (1 Ate 5:18)

### F13.2 Kodi kuthokoza nkofunika?

Inde; pamene Ambuye anachiritsa akhate khumi aja, mmodzi yekha ndi amene anabwerera kukathokoza. Ambuye anakondwera naye, koma osati asanu ndi anai ena aja. \_\_\_Iye anati; " Kodi sanakonzedwa khumi? Koma ali kuti asanu ndi anai aja? Akubwera kulemekeza Mulungu sanapezeka mmodzi kodi, koma mlendo uyu?" (Mat 17:17-18)

### F13.3 Tisonyeze bwanji kuthokoza kwathu kwa Mulungu?

Pothokoza m'dzina la Ambuye athu Yesu Khristu. \_\_\_"Potero mwa Iye tipereke nsembe yakuyamika Mulungu, ndiyo chipatso cha milomo yovomereza dzina lake." (Ahe 13:15; onaninso Aro 1:8; Ako 3:17; Mas 100:4)

### F13.4 Kodi tithokoze Mulungu chifukwa cha anzathu okhulupilira?

Inde ndithu. Tikhale ngati mtumwi Paulo amene anauza Afilipi kuti: "Ndiyamika Mulungu wanga pokumbukira inu ponse." (Afi 1:3)

### F13.5 Kodi nkofunika kuthokoza tisanalandire chakudya?

Inde; Ambuye athu Yesu Khristu anathokoza asanadye. \_\_\_Mwachitsanzo, pamene anadyetsa anthu 4 000, "Ndipo analamula anthu akhamulo akhale pansu; natenga mikate isanu ndi iwiriyo, nayamika, nanyema, napatsa ophunzira ake, kuti apereke kwa iwo; ndipo anapereka kwa khamulo." (Mk 8:6)

### F13.6 Kodi mau ndiyo njira yokhayo yothokoza Mulungu?

Ayi; moyo wathu watsiku ndi tsiku wa chikhristu ukuyenera kukhala wothokoza. \_\_\_"Chifukwa chake monga momwe munalandira Khristu Yesu Ambuye, muyende mwa Iye: ozika mizu ndiomangirika mwa Iye, ndi okhazikika m'chikhulupiliro, monga munaphunzitsidwa, ndi kuchulukitsa chiyamiko." (Ako 2:6-7) "ndi chokhachi, kumene tidafikirako, mayendedwe athu alinganeko." (Afil 3:16)

### F13.7 Kodi tithokoze anzathu amene atichitira zabwino?

Inde, tikuyenera kutsata chitsanzo cha anthu a Mulungu a m'Baibulo. \_\_\_Mwacchitsanzo, tiyenera kutsatira Davide, amene anauza Solomoni kuti, "Koma uchitire zokoma ana amuna aja a Barizilai wa ku Gileadi, akhale pakati pa akudyera pa gome lako, popeza momwemo amandiyandikira muja ndinalikuthawa Abisalomu mbale wako." (1 Maf 2:7)

## PHUNZIRO 14: KUKHULULUKA

### F14.1 Chifukwa chiyani tiyenera kukhululukirana?

Chifukwa Mulungu mwini adatikhululukira. \_\_\_”Koma mukhalirane okoma wina ndi mzake, a mtima wa chifundo akukhululukirana nokha, monganso Mulungu anakhululukira inu.” (Aef 4:32)

### F14.2 Mukhululukire ndani?

Aliyense amene adza kwa ine ndi mtima wolapa. \_\_\_”Kadzichenjerani nokha; akachimwa mbale wako, umdzudzule; akalapa, umkhululukire.” (Luk 17:3)

### F14.3 Mbale wanga akandichimwira, ndimkhululukire kangati?

Nthawi zonse pamene wabwera kudzandipempha kuti ndimkhululukire. \_\_\_Pamenepo Petro anadza, nati kwa Iye, “Ambuye, mbale wanga adzandilakwira kangati, ndipo ine ndidzamkhululukira iye? kufikira kasanu ndi kawiri kodi?” Yesu ananena kwa iye, “Sindinena kwa iwe kifikira kasanu ndi kawiri koma kufikira makumi asanu ndi awiri kubwezedwa kasanu ndi kawiri.” (Mateyu 18:21-22)

### F14.4 Nanga ngati mbale wako atamabwerezabwereza kukuchimwira?

Ndiyenera kumukhululukirabe popeza Mulungu adati, “ndipo akakuchimwira kasanu ndi kawiri pa tsiku lake, nakakutembenukira kasanu ndi kawiri ndi kunena, 'Ndalapa ine', uzimkhululukira.” (Luk 17:4)

### F14.5 Nanga utakana kumukhululukira wina?

Ngati ndikakamira osamukhulukilira mzanga, sindikhalanso mwana wa Mulungu. \_\_\_ Mulungu akuti: “Pakuti ngati mukhululukira anthu zolakwa zawo adzakhululukira inunso Atate wanu wa Kumwamba. Koma ngati simukhululukira anthu zolakwa zawo, Atate anunso sadzakhululukira zolakwa zanu.” (Mat 6:14-15); onaninso Mk 11:25-26)

### F14.6 Nanga ngati wina amene wandichimwira sandipempha kuti ndimukhululukire?

Sindiyenera kumusungira chidani kapena kuganiza zomubwezera. \_\_\_Popeza Ambuye akuti: “Kubwezera kuli kwanga, Ine ndidzabwezera, ati Ambuye.” (Aro 12:19) ndipo Yakobo akuti: Musaipidwe wina ndi mzake, abale kuti mungaweruzidwe. Tawonani woweruza aima pakhomo.” (Yak 5:9)

## PHUNZIRO 15: MKWIYO

### F15.1 Kodi mkwiyo ulionse ndi tchimo?

Ayi; popeza ngakhale Ambuye Yesu omwe adakwiya koma sadachimwe.(Mk 3:5; Ahe 3:15), komanso Paulo akunena kuti; “Kwiyani, koma musachimwe.” (Aef 4:26a)

### F15.2 Kodi mkwiyo umasanduka bwanji kukhala tchimo?

Pamene ndidzikonda, ndikwiya popanda chifukwa chenicheni, kapena ndikwiya kopambana muyeso. \_\_\_Ambuye Yesu akuti; “Munamva kuti kunanenedwa kwa iwo akale, Usaphe; koma yense wakupha adzakhala wopalamula mlandu. Koma ine ndinena kwa inu, kuti yense wokwiwira mbale wake wopanda chifukwa adzakhala wopalamula mlandu.” (Mat 5:21-22a)

### F15.3 Kodi ndi bwino kusunga mkwiyo masiku ambiri pachifukwa china chirichonse?

Ayi, chifukwa satana adzangopezepo mwayi pa ine. \_\_\_”Dzuwa lisalowe muli chikwiwira, ndiponso musampatse malo mdierekezi.” (Aef 4:26b-27)

### F15.4 Muchite chiyani ngati wina achita chinthu chokupsetsani mtima?

Ndikuyenera kudziletsa. \_\_\_”Wosakwiya msanga aposa wamphamvu; wolamulira mtima wake naposa wolanda mudzi. (Miy 16:32)

### F15.5 Nanga ngati wina atakupsetsani mtima?

Ndisakwiye, ndipo ndingoziponya kunkhongo ngati nkotheke kutero. \_\_\_”Kulingalira kwa munthu kuchedwetsa mkwiyo; ulemelero wake uli wakuti akhululukire cholakwa. “ (Miy 19:11)

### F15.6 Mungatani kuti mupewe mikangano yobweretsa mkwiyo ndi anzanu?

Osamuyankha mzathu amene wakwiya ndi mau amkwiyo. \_\_\_”chitsiru chivumulutsa mkwiyo wake onse, koma wanzeru auletsa nautontholetsu.” (Miy 29:11)

### F15.7 Ngati ukukangana ndi mnzako, ungachite chiyani pofuna kuthetsa mkanganowo?

Poyankhula pang'onopang'ono ndi modekha. \_\_\_”Mayankhidwe ofatsa abweza mkwiyo; koma mau owawitsa aputa nsunamo.” (Miy 15:1)

### F15.8 Kodi nkofunika kuthetsa mkangano ndi anzanu msanga?

Inde; sindikuyenera kulola kuti mkangano upitilire. \_\_\_”chiyambi cha ndeu chifanana ndi kutsegulira kwa madzi; tsono kupikisana kusanayambe, tasiya makani.(Miy 17:14)

### F15.9 Ngati wina wakukwiwira utani naye?

Ndiyeseke kuti ndiyanjane naye (Mat 5:23-24; 18:15); ndipo mphatso ingathe kuthandiza, popeza, “Mphatso ya mseri ipembedza mkwiyo.” (Miy 21:14)

## PHUNZIRO16: KUKHULUPIRIKA NDI UDINDO

### F16.1 Kodi chikhulupiliro chifanana ndi kukhulupirika?

Ayi; chikhulupiliro ndi kumvera pamene kukhulupilira ndi kukhala woona pa zomwe talonjeza kapena udindo wathu. \_\_\_ “Mulungu ndi wokhulupilika chifukwa amasunga malonjezo ake, monga momwe mlembi wa Masalimo akunenera: “Ndidzayimbira za chifundo za Yehova nthawi zonse. Pakamwa panga ndidzadzawitsira chikhulupiliro chanu ku mibadwo mibadwo.” (Mas 89:1)

### F16.2 Tingaphunzire kukhulupirika ndi kukhala ndi udindo kuchokera kwa yani?

Kuchokera kwa Ambuye Yesu amene anakhala wokhulupirika kwa Atate ake nthawi zonse. \_\_\_ “Amene (Ambuye Yesu) anakhala wokhulupirika kwa Iye (Atate) amene adamuikayo, monganso Mose m'nyumba yake yonse.” (Ahe 3:2)

### F16.3 Kukhala mtumiki wokhulupirika wa Mulungu ndiko kutani?

Ndiko kupereka moyo wanga mmanja mwa Mulungu pogwiritsa ntchito mphatso zosiyanasiyana zomwe Iye wandipatsa. \_\_\_ Mufanizo la matalente lomwe Ambuye Yesu anapereka, mbuye uja anati kwa kapolo wake, “Chabwino, kapolo iwe wabwino ndi wokhulupirika pa zinthu zazing'ono, ndidzakhazika iwe pa zinthu zambiri; lowa iwe mchikondwerero cha mbuye wako.” (Mat 25:21 onaninso vesi 23)

### F16.4 Kukhala wokhulupirika mmalankhulidwe ndiko kutani?

Ndiko kunena zoon. \_\_\_ “Mboni yokhulupirika siidzanama; koma mboni yonyenga imalankhula zonama.” (Miy 14:5)

### F16.5 Kukhala wokhulupirika kwa okhulupilira anzathu ndiko kutani?

Ndiko kuwathandiza. \_\_\_ Mtumwi Yohane akuyamikira Gaiya: \_\_\_ “Wokondeka, uchite mokhulupirika chirichonse chimene uwachitira abale onse, ngakhale alendo ( ngakhale kuti ndi alendo)” (3 Yoh 5)

### F16.6 Kukhala okhulupirika pakhomo ndiko kutani?

Ndiko kukhala ndi udindo ngakhale pazazing'ono monga kugwira ntchito za pakhomo panga komanso kusamala chipida changa chogona. \_\_\_ “Iye amene ali wokhulupirika m'chaching'ono alinso wokhulupirika m'chachikulu; ndipo amene ali osalungama m'chaching'ono, alinso wosalungama m'chachikulu.” (Luk 16:10)

### F16.7 Mukakhala wokhulupirika pakhomo panu, mudzapindula chiyani?

Makolo anu adzakukhulupilirani ndipo simudzasowa mtendere. \_\_\_ Wansembeyo anawakhulupilira onse anagwira ntchito mokhulupirika mmasiku a Yowasi, popeza “Sanawerengera anthu amene anapereka ndalamazi mmanja mwawo kuti apatse ogwira ntchito ; popeza anachita mokhulupirika. (2 Maf 12:15)

### F16.8 Kodi kukhulupirika kutipindulitsa pa moyo uno?

Inde; \_\_\_ “Munthu wokhulupirika ali ndi madalitso ambiri; koma wokangaza kulemera sadzapulumuka chilango.” (Miy 28:20)

## PHUNZIRO 17: KUKHULUPIRIKA

### F17.1 Kodi kukhulupirika ndi ungwiro wa chikristu?

Inde; koma kukhulupirika kwake kukhale kwa chikondi kwa anzathu, kumpingo, kapena kudziko pa nthawi ya mavuto. \_\_\_”Bwenzi limakonda nthawi zonse; ndipo mbale anabadwira kuti akuthandize pooneka tsoka. (Miy 17:17)

### F17.2 Tiphunzira kwa yani kukhala bwenzi lokhulupirika?

Kuchokera kwa Yesu Khristu. \_\_\_Solomoni akukamba za Yesu pamene akuti: “Woyanjana ndi ambiri angodziononga; koma liripo bwenzi lipambana ndi mbale kuumirira.” (Miy 18:24)

### F17.3 Kukhulupirika kwa mzako pamene ali mmavuto nkutani?

Ndi kumteteza , munga momwe Jonatani anatetezera Davide pamene bambo wake Sauli anafuna kumupha. \_\_\_”Ndipo Jonatani analankhula ndi atate ake movomereza Davide, nanena naye, Mfumu asachimwire mnyamata wake Davide; chifukwa iyeyo sanachimwira inu, ndipo ntchito zake anakuchitirani zinali zabwino ndithu.” (1 Sam 19:4)

### F17.4 Kodi kukhulupirika kwa mzathu pamene wachimwa nkutani?

Ndi kumuchenjeza mwa chikondi. \_\_\_”Chidzudzulo chomveka chiposa chikondi chobisika. Kulasa kwa bwenzi kuli kokhulupirika; koma mdani apsopsona kawirikawiri. (Miy 27:5-6)

### F17.5 Kukhulupirika kwa amene atiuza za chinsinsi nkutani?

Ndi kusunga chinsinsi. \_\_\_”Kazitape woyendayenda amawanditsa zinsinsi; koma wokhulupirika mtima abisa mau.” (Miy 11:13)

### F17.6 Ziripo zitsanzo m'Buku Lopatulika za kukhala wokhulupirika ku boma?

Inde; Davide anamusiya Sauli osamupha ngakhale kuti Sauliyo anafuna kumupha Davide. \_\_\_”Davide anati kwa Sauli, “Onani lero lomwe maso anapenya kuti Yehova anakuperekani inu mdzanja langa mphangamo, ndipo ena anandiuza , ndikupheni ; koma ndinakulekani , ndi kuti, sindidzatukulira mbuye wanga dzanja langa; chifukwa iye ndiye wodzozedwa wa Yehova.” (1 Sam 24:10)

### F17.7 Kodi Baibulo litiletsa kusakhulupirika?

Inde. \_\_\_”Kukhulupirira munthu wachiwembu tsiku la tsoka kunga dzino lothyoka ndi phazi loguluka.” (Miy 25:19)

### F17.8 Kukhulupirika kwathu kulekezere pati?

Kufikira pamene chikondi chiri cholungama ndi chowona, popeza chikondi “Sichikondwera ndi chinyengo, koma chikondwera ndi choonadi. (1 Akor 13:6)

## PHUNZIRO 18: CHIKHALIDWE CHABWINO NDI KUSUNGA MWAMBO

### **F18.1 Kodi kuchita zinthu mwa dongosolo ndi ungwiro wa chikhristu?**

Inde; Mtumwi Paulo akutilamula kuti: “Koma zonse zichitike koyenera ndi kolongosoka.” (1 Ako 14:40)

### **F18.2 Kusunga mwambo kukugwirizana ndi kuchita zinthu mwadongosolo?**

Inde; kusunga mwambo ndiko kusamala za khalidwe lathu labwino. \_\_\_Mtumwi Paulo anadziwa za kufunika kwa kusunga mwambo. Iye akuti: “Koma ndipumphuntha thupi langa , ndipo ndiliyesa kapolo; kuti kapena ngakhale ndalalikira kwa ena, ndingakhale wotayika ndekha.” (1 Ako 9:27)

### **F18.3 Kodi moyo wosachita zinthu mwadongosolo ndi tchimo?**

Inde; Mtumwi Paulo anauza Atesalonika kuti asiyane nawo abale awo wosasunga mwambo . \_\_\_”Ndipo tikulamulani, abale, m'dzina la Ambuye wathu Yesu Khristu, kuti mubwevuke kwa mbale yense wakuyenda dwakedwake, wosatsata mwambo umene anaulandila kwa ife.”(2 Ate 3:6)

### **F18.4 Kodi nkofunika kusunga mwambo pa moyo wathu?**

Inde; popeza Ambuye akuti, “Wopereka nsembe ya chiyamiko andilemekeza ine; ndipo kwa iye wosunga mayendedwe ake , ndidzamuonetsa chipulumutso cha Mulungu. “ (Mas 50:23)

### **F18.5 Kodi Ambuye Yesu adatiwonetsa chitsanzo cha kuchita zinthu mwa dongosolo?**

Inde; pamene anadyetsa anthu 5 000. \_\_\_”Ndipo anawalamula kuti akhalitse pansi onse mmagulu magulu pamsipu. Ndipo anakhala pansi mabungwe mabungwe a makumi khumi, ndi a makumi asanu. (Marko 6:39-40)

### **F18.6 Kodi Yesu adatiwonetsa chitsanzo cha kukhala wosunga mwambo?**

Inde; tsiku ndi tsiku ankadzuka mmamawa kukapemphera . \_\_\_ Marko akuti: “Ndipo mmamawa mwake anauka usikusiku, naturuka namuka kuchipululu, nakapemphera kumeneko. (Marko 1:35)

### **F18.7 Perekani njira imodzi yomwe mungalimbikitsire moyo wosunga mwambo.**

Zanga zonse zimathera kwa Ambuye: \_\_\_”Mmamawa, Yehova, mudzamva mau naga; Mmawa ndidzakukonzerani pemphero langa, ndipo ndidzadikira. (Mas 5:3)

### **F18.8 Mungakhazikitse bwanji khalidwe lochita zinthu mwadongosolo mmoyo wanu wachikhritu?**

Ndidzayesetsa kukhala wadongosolo ndi waukhondo pa zonse zomwe ndichita pakhomu panga, kusukulu, ndi ku tchalitchi. \_\_\_”Pakuti Mulungu sali Mulungu wa chisokonezo.” (1 Ako 14:33)

## PHUNZIRO 19: KUDEKHA MTIMA DI KUPILIRA

### **F19.1 Kodi kudekha (kudikilira ndi mtima wachimwemwe) ndi kupilira (kukhala mmasautso mosangalala) ndi ungwiro wa chikhsritu?**

Inde; Mtumwi Paulo anapempherera Akolose kuti akhale “Olimbikitsidwa m'chilimbiko chonse monga mwa mphamvu ya ulemelero wake, kuchitira chipiliro chonse ndi kuleza mtima konse pamodzi ndi chimwemwe.” (Ako 1:9-11)

### **F19.2 Tingaphunzire kwa yani kudekha mtima ndi kupilira?**

Kwa Ambuye Yesu. \_\_\_”Chifukwa chake ifenso, popeza tizingidwa nawo mtambo waukuru chotere wa mboni, titaye cholemetsa chirichonse, ndi tchimoli limangotizinga ndipo tithamange mwachipiliro makaniwo adatiikira, ndi kupenyenera woyambira ndi womaliza wa chikhulupiliro chathu, Yesu, ameneyo, chifukwa cha chimwemwe choikidwa pamaso pake, anapirira mtanda, nanyoza manyazi, nakhala padzanja lamanja la mpando wachifumu wa Mulungu.” (Ahe 12:1-2)

### **F19.3 Ambuye anaonetsa bwanji kudekha mtima ndi kupilira?**

“Iye anatsenderezedwa, koma anadzichepetsa yekha osatsegula pakamwa pake; ngati nkhosa yotsogoleredwa kukaphedw, ndi ngati mwana wa nkhosa amene ali du pamaso pa omsenga, motero sanatsegula pakamwa pake.” (Yes 53:7)

### **F19.4 Tiphunziranso kwa yani wina kudekha mtima ndi kupilira?**

Kuchokera kwa Yobu ndi aneneri. \_\_\_”tengani, abale, chitsanzo chakumva zowawa ndi kuleza mtima, aneneri amene analankhula mdzina la Ambuye. Tawonani tiwayesa odala opirirawo; mudamva za chipiliro cha Yobu ....” (Yak 5:10-11a)

### **F19.5 Kodi Akhristu apilire bwanji?**

Mosangalala ndi modekha. \_\_\_”Muchiyese chimwemwe chokha, abale anga, mmene mukugwa mmayesero a mitundu mitundu; pozindikira kuti chiyesedwe cha chikhulupiliro chanu chichita chipiliro. Koma chipiliro chikhale nayo ntchito yake yangwiro kuti mukakhale a ngwiro ndi opanda chilema, osasowa kanthu konse.” (Yak 1:2-4; onaninso Aro 5:3-4 ; 1 Pet 2 : 20)

### **F19.6 Kodi tisiye kuchita zabwino chifukwa choti anthu ena satiyamikira?**

Ayi; Paulo Mtumwi akuti: “Koma tisaleme pakuchita zabwino; pakuti panyengo yake tidzatuta tikapanda kufooka.” (Aga 6:9)

### **F19.7 Kukhala moyo wa chikhristu ndi kuphunzira katekisimu ndi zovuta zedi, choncho mukutani?**

Khalani wodekha mwa Ambuye. \_\_\_”Nkokoma kuti munthu ayembekeze ndi kulindira modekha chipulumutso cha Yehova. Nkokoma kuti munthu asenze goli ali wamng'ono.” (Maliro 3:26-27)

### **F19.8 Mulungu nthawi ina saoneka ngati kuti akumva madandaulo anu, nanga mungatani?**

Dikiranibe. \_\_\_”Kuyembekezera ndayembekezera Yehova; ndipo anandilora, namva kufuula kwanga.” (Mas 40:1, onaninso Mas 37:7)



## PHUNZIRO 20: KUGWIRA NTCHITO MOLIMBIKA NDI MOSAMALA

### F20.1 Kodi kugwira ntchito molimbika ndi mosamala ndi ungwiro wa chikristu?

Inde; popeza Malembo atiuza kuti; “Chirichonse dzanja lako lichipeza kuchichita; uchichite ndi mphamvu zako. (Mla 9:10)

### F20.2 Malembo akutiphunzitsa kugwira ntchito molimbika ndi mosamala kuchokera kuti?

Kwa nyererere. \_\_\_”Pita kunyerere waulesi iwe; penya njira zawo nuchenjere,; ziribe mfumu, ngakhale kapitawo, ngakhale mkulu; koma zitengeratu zakudya zawo mmalimwe; nizituta dzinthu dzawo mmasika. (Miy 6:6-8)

### F20.3 Ntchito zanu za kunyumba, kusukulu kapena ku tchalitchi, muzigwire ndi mtima wotani?

“Chirichonse mukachichita, gwirani ntchito mochokera mumtima, monga kwa Ambuye, osati kwa anthu ayi.” (Akol 3:23)

### F20.4 Chotilimbikitsa kugwira ntchito molimbika ndi mosamala ndi chiyani?

Titumikira Mulungu ndi zinthu zathu. \_\_\_Mwa chitsanzo, tidzatha kuthandiza osowa; popeza Paulo akuti: “Wakubayo asabenso; koma makamaka agwiritse ntchito, nagwire ntchito yokoma ndi manja ake, kuti akhale nacho chakuchereza osowa.” (Aef 4:28 onaninso Mac 20:35)

### F20.5 Mulungu amalipira, mmoyo uno, amene agwira ntchito molimbika?

Inde, popeza Solomoni akuti, “kodi upenya munthu wofulumiza ntchito zake? adzaima pamaso pa mafumu, osaima pa maso pa anthu achabe.” (Miy 22:29)

### F20.6 Kodi ulesi umabala chiyani?

Umphawi ndi moyo womvetsa chisoni. \_\_\_”Tulo pang'ono, kungoodzera pang'ono, kungomanga manja pang'ono nkugona, ndipo umphawi wako udzafika ngati mbala; ndi kusauka kwako ngati munthu wachikopa. “ (Miy 24:33-34)

### F20.7 Kodi tikuyenera kugwira ntchito tsiku lililonse?

Ayi; tiyenera kupuma tsiku la sabata, ndi kulisunga kukhala loyera. \_\_\_”Koma tsiku la chisanu ndi chiwiri ndilo sabata la Yehova Mulungu wako; usagwire ntchito iriyonse, kapena iwe wekha, kapena mwana wako wa mwamuna, kapena mwana wako wamkazi, kapena wantchito wako wamwamuna kapena wantchito wako wamkaz, kapena nyama zako, kapena mlendo amene ali mmudzi mwako.” (Eks 20:10)

### F20.8 Ndiye kuti sitisowa kulimbika pa zochitika za pa tsiku la sabata?

Ayi; tikuyenera kulimbika ntchito zonse ngakhale zachifundo. \_\_\_”Kondwerani mchiyembekezo, pilirani mmasautso; limbikani chilimbikire nkupemphera.” (Aro 12:12)

## PHUNZIRO 21: NZERU

### F21.1 Kodi nzeru ndi ungwiro wa chikhristu?

Inde; nzeru ndikuganiza mwa umungu. \_\_\_”Kumuopa Yehova ndiko chiyambi cha nzeru: Onse akuchita chotero ali nacho chidziwitso chokoma; chilemekezo chake chikhalitsa kosatha.” (Mas 111:10)

### F21.2 Tingathe kudziwa zinthu, koma tingathe kupeza nzeru?

Inde, nzotheka, \_\_\_”Nzeru ipambana, tatenga nzeru; mkutenga kwako konseko utenge luntha.” (Miy 4:7)

### F21.3 Mungapeze bwanji nzeru?

Kuchokera mMawu a Mulungu omwe tawawerenga ndi kuwamva. \_\_\_”Pakuti Yehova apatsa nzeru; kudziwa ndi kuzindikira kuturuka mkamwa mwake.” (Miy 2:6; onaninso Miy 5:1)

### F21.4 Kodi kumva ndi kuwerenga kokha nzokwanira kupeza nzeru?

Ayi; ndikusowa kepempha kwa Mulungu kuti andipatse nzeru. \_\_\_”Koma wina wa inu ikamsowa nzeru, apemphe kwa Mulungu amene apatsa kwa onse modzala manja, ndiwosatonza ndipo adzampatsa iye.” (Yak 1:5 komanso 2 Mbi 1:7-12)

### F21.5 Mungakhale bwanji mwanzeru?

Potsatira malamulo a Mulungu. \_\_\_”Malamulo anu andipatsa nzeru yakuposa adani anga; pakuti akhala nane chikhalire.” (Mas 119:98)

### F21.6 Nanga ngati nthawi zina simukudziwa kuti mugwiritsa ntchito malamulo ati ndipo palibe oti mumfune, muchite chiyani?

Ndipemphere ndikuganizira zomwe Mulungu angafune kuti ndichite pa nthawi imeneyo. \_\_\_”Chiyambi cha nzeru ndi kuopa Yehova; kudziwa Woyerayo ndiko luntha.” (Miy 9:10 onaninso Miy 1:7)

### F21.7 Mayi ndi bambo anu amakuthandizani bwanji kuti mukule munzeru?

Amandilangiza ndikachita zosayenera kapena ndikachimwa. \_\_\_”Nthyole ndi chidzudzulo zipatsa nzeru; koma mwana womulekelera achititsa amake manyazi.” (Miy 29:15)

### F21.8 Kodi nzeru nzofunika kuti mukhale moyo wosangalala wachikhristu?

Inde, \_\_\_”Wodala ndi wopeza nzeru, ndi woona luntha.” (Miy 3:13)

### F21.9 Kodi nzeru nzofunika kuti mukhale ndi ubale wabwino ndi anzanu?

Inde; popeza “Wopeputsa mzake asowa nzeru; koma wozindikira amatonthola.” (Miy 11:12)

## PHUNZIRO 22: KUYERA MTIMA

### F22.1 Kuyera mtima ndi kutani?

Ndikukhala ndi makhalidwe abwino mmalankhulidwe, mmachitidwe ndi mmaganizo kuti ndifanefane ndi Ambuye Yesu Khristu, koma ndisiyane ndi dziko la pansi. \_\_\_"Komatu monga lye wakuitana inu ali woyera mtima, khalani inunso woyera mtima mmakhalidwe anu onse popeza kwalembedwa: Mudzikhala woyera mtima popeza lne ndine woyera mtima." (1 Pet 1:15-16)

### F22.2 Kodi mkhristu aliyense sali woyera mwa Khristu Yesu?

Inde, talungamitsidwa mwa Khristu ndipo choncho ndife 'wopatulika' kutanthauza kuti 'woyera'; koma tili ndi udindo wokhala moyo wopatulika. \_\_\_"Londolani mtendere ndi anthu onse, ndi chiyeretso chimene akapanda ichi, palibe mmodzi adzaona Ambuye." (Ahe 12:14)

### F22.3 Munthu wolungamitsidwa angathe kukhala wosayera mtima?

Ayi; munthu wolungamitsidwa mwa Khristu amakula mkuyera. Amene anena kuti ndi wolungamitsidwa koma alibe kuyera ameneyo ngonama. \_\_\_"Pakuti ichi muchidziwe kuti wadama yense, kapena wachidetso, kapena wosilira, amene apembedza mafano, alibe cholowa mu ufumu wa Khristu ndi Mulungu. (Aef 5:5)

### F22.4 Kodi munthu akuyenera kubadwanso kachiwiri kuti akhale woyera?

Inde; munthu wolungamitsidwa ndi wobadwanso kachiwiri. \_\_\_Paulo Mtumwi akunena kwa obadwanso kachiwiri pamene akuti: "Koma tsopano pamene munamasulidwa kuuchimo, ndi kukhala akapolo a Mulungu, muli nacho chobala chanu chakufikira chiyeretso, ndi chimaliziro chake moyo wosatha." (Aro 6:22)

### F22.5 Mungakule bwanji mchiyero?

Pakuwerenga ndi kumva mawu a Mulungu. \_\_\_"Ambuye Yesu anapemphera: "Patulani iwo mchoonadi; mau anu ndi choonadi." ( Yoh 17:17); ndipo Mtumwi Paulo akuti: "Lemba lililonse adaliuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa pa chiphunzitsa, chitsutsano, chikonzero, chilangizo cha mchilungamo: Kuti munthu wa Mulungu akhale woyenera, wokonzeka kuchita ntchito iri yonse yabwino." ( 2 Tim 3:16-17)

### F22.6 Kupatulapo kuwerenga ndi kumva Mawu a Mulungu, mungachite chiyani kuti mukule mchiyero?

Ndikuyenera kuchita zomwe Mawuwo anena. \_\_\_"Chifukwa chake ndikukupemphani inu abale, mwa zifundo za Mulungu, kuti mupereke matupi anu nsembe yamoyo, yopatulika, yokondweretsa Mulungu, ndiko kupembedza kwanu koyenera. Ndipo musafanizidwe ndi makhalidwe a pansi pano: koma mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu, kuti mukazindikire chimene chiri chifuno cha Mulungu, chabwino, ndichokwondweretsa ndi chamgwiro. (Aro 12: 1-2)

## PHUNZIRO 23: KUDZILETSA

### F23.1 Kodi kudziletsa ndi ungwiro wa chikristu?

Inde; ndi chinthu chimene mkristu aliyense akuyenera kukhala nacho. \_\_\_”Ndipo mwa “Ichi chomwe, pakutengeraponso changu chonse, muonjezerepo kukoma pa chikhulupiro chanu, ndi pakukoma chizindikiritso; ndi pachizindikiritso chodziletsa; ndi pa chodziletsa chipiliro; ndi pa chipiliro chipembedzo; ndi pa chipembedzo chikondi cha pa abale. Pakuti izi zikakhala ndi inu, ndipo zikachulukana zidzachita kuti musakhale aulesi kapena opanda zipatso za chizindikiritso cha Ambuye wathu Yesu Khristu.” ( 2 Pet 1:5-8)

### F23.2 Kodi kudziletsa ndi chizindikiro cha chaulere?

Inde; amene wabadwanso kachiwiri akuyenera kudziletsa ku zikhumbokhumbo zoipa ndi zilakolako za dama. \_\_\_”Koma chipatso cha Mzimu Woyera ndicho chikondi, chimwemwe, mtendere, kuleza mtima, chifundo, kukoma mtima, chikhulupiro, chifatso, chiletso; pokana zimenezi palibe lamulo.” (Aga 5:22-23)

### F23.3 Mungaphunzire bwanji kudziletsa?

Podziwa mumtima mwanga kuti ine ndine wake wa Ambuye. \_\_\_”Koma valani inu Ambuye Yesu Khristu, ndipo musaganizire za thupi kuchita zofuna zake.” (Aro 13:14)

### F23.4 Tingaphunzire kudziletsa kuchokera kwa yani?

Mneneri Daniel. \_\_\_”Koma Daniel anatsimikiza mtima kuti asadzidetse ndi chakudya cha mfumu, kapenandi vinyo amamwa; chifukwa chake anapempha mkulu wa adindo amlole asadzidetse.” (Dan 1:8)

### F23.5 Ndi nthawi iti yomwe, monga mwana, ndikuyenera kudziletsa?

Nthawi iriyonse yomwe ndikusangalala pamene ndichita mobzola muyezo ndi kuchimwira Mulungu, kuwononga nthawi yanga pachabe kapena kugwiritsa ntchito thupi langa mosayenera: mwachitsanzo, kuwonera TV, kusewera mopambana muyezo, kudya maswiti ambiri. \_\_\_Solomoni akuti, “Wapeza uchi kodi? Idyapo wokwanira, kuti ungakukole nusanze.” (Miy 25:16)

### F23.6 Kodi mukuyenera kudziletsa pamene mukucheza ndi ena?

Inde, ndiyenera kuletsa mkwiyo ndi lilime langa pamene wina wandikwiyitsa. \_\_\_”Chitsiru chivumbulutsa mkwiyo wake onse, koma wanzeru auletsa nautonthoza.” (Miy 29:11)

### F23.7 Ndi mbali iti ya moyo wanu pamene mukuyenera kudziletsa kwathunthu kuti mukule bwino?

Pakukhala moyo wolewa machimo. \_\_\_”Thawani dama. Tchimo liri lonse munthu akalichita liri kunjwa kwa thupi; koma wachiwerewere achimwira thupi lake la iye yekha.” (1 Ako 6:18)

## PHUNZIRO 24: KUPEMPHERA

### F24.1 Kodi kupemphera ndi moyo wa ngwiro wa chikristu?

Inde, moyo wopemphera ndi umboni weniweni wakutembenuka mtima. \_\_\_"Yehova ali pafupi ndi onse akuitanira kwa lye, onse akuitanira kwa lye mchoonadi." (Masalimo 145:18)

### F24.2 Kodi anthu osakhulupilira samapemphera nawonso mwakhama?

Inde; koma amapemphera mafano kapena milungu yonama. \_\_\_Munthu wongolengedwa chabe sadzatchula Mulungu wa moyo ndi woona: "Pakuti ife tonse takhala ngati wina amene ali wosakonzeka; ndi zolungama zathu zonse ziri ngati chovala chodetsedwa; ndipo ife tonse tifota ngati tsamba, ndi zoipa zathu zitiuluzwa monga mphepo." (Yes 64:6-7a)

### F24.3 Tingalimbikitse bwanji moyo wamapemphero?

Njira ina imodzi ndi kudzuka mmamawa tsiku liri lonse ndi kupemphera monga ankachitira Ambuye Yesu. \_\_\_"Ndipo mmamawa wake anauka naturuka namuka kuchipululu, nakapemphera kumeneko." (Marko 1:35)

### F24.4 Mupemphere mmamawa wokha?

Ayi, ndikuyenera "Kupemphera mosalekeza." (1 Ate 5:17)

### F24.5 Kupemphera kosalekeza ndiko kutani?

Ndikupemphera nthawi iriyonse pamene tingathe kutero. Ndikukhalanso ndi dongosolo labwino la moyo wa mapemphero monga anachitira mneneri Daniel. \_\_\_"(Danieli) anagwada maondo ake tsiku limodzi katatu, napemphera, navomereza pamaso pa Mulungu wake monga umo anachitira kale lonse." (Dan 6:10)

### F24.6 Kodi mukuyenera kuwerama ndi kutseka maso popemphera?

Ayi; Nehemiya akutipatsa chitsanzo chabwino cha kupemphera asanayankhe funso la mfumu. \_\_\_"Ndipo mfumu inati kwa ine: Ufunanji iwe? Pamenepo ndinapemphera Mulungu wa Kumwamba. Ndipo ndinati kwa mfumu..." (Neh 2:4-5)

### F24.7 Nanga ngati simukudziwa mmene mungapempherere kapena choti mupemphe?

Mzimu woyera adzandithandiza. \_\_\_"Ndipo momwemonso Mzimu athandiza kufoka kwathu; pakuti chimene tizipempha monga chiyenera, sitidziwa; koma Mzimu mwini atipempherera ndi zobuula zosatheka. Ndipo lye amene asanthula mmitima adziwa chimene achisamalira Mzimu, chifukwa apempherera oyera mtima monga mwa chifuno cha Mulungu." (Aro 8:26-27)

## PHUNZIRO 25: KULINGALIRA MOZAMA

### F25.1 Kodi nkofunika kulingalira mozama?

Inde, Mtumwi Yohane akunena kuti: \_\_\_"Okondedwa, musamakhulupilira mzimu uliwonse, koma yesani mizimu ngati ichokera mwa Mulungu: popeza aneneri onyenga ambiri anaturuka kulowa m'dziko lapansi." (1 Yoh 4:1)

### F25.2 Kodi Ambuye Yesu sadanene kuti "Musaweruze, kuti nanu musaweruzidwe?"

Inde, ndipo akutinso: Musaweruze monga maonekedwe, koma weruzani chiweruzo cholungama." (Yoh 7:24)

### F25.3 Chimachitika nchiyani ngati sitilingalira mozama?

Tingasokere mosavuta. \_\_\_Tikhala ngati "makanda, ogwedezekagwedezeka, natengekatengeka ndi mphepo yonse ya chiphunzitsa, ndi tsenga la anthu, ndi kuchenjerera kukatsata chinyengo cha kusokeretsa." (Aef 4:14)

### F25.4 Mungaphunzire bwanji kulingalira mozama?

"Yesani zonse; sungani chokomacho." (1 Ate 5:21)

### F25.5 Mungayese bwanji zinthu zonse?

Poyerekeza ndi mau a Mulungu. \_\_\_"Kuchilamulo ndi kuumboni ngati iwo sanena malinga ndi mau awa, ndithu sadzaona mbandakucha." (Yes 8:20)

### F25.6 Mungagwiritse ntchito bwanji Mau a Mulungu kuti muyese zinthu zonse?

Pobisa Mau a Mulungu ndi maphunzitsa a katekisimu mu mtima mwanga. \_\_\_"Ndinawabisa mau anu mumtima mwanga, kuti ndisalakwire inu." (Mas 119:11)

### F25.7 Mungaphunzirenso bwanji kulingalira mozama?

Mulungu watipatsa abusa ndi aphunzitsi kuti atithandize kukhwima muuzimu ndi kulingalira mozama. Ndidzaphunzira kuchokera kwa iwo; ndidzayerekeza maphunzitsa awo ndi mau a Mulungu. Ndidzakhala ngati ngati a Bereya. \_\_\_"Amenewa anali mfulu koposa a m'Tesalonika, popeza analandira mau ndi kufunitsa kwa mtima wonse nasanthula m'malembo masiku onse, ngati zinthu zinali zotero." (Mac 17:11)

### F25.8 Kodi alipo aphunzitsi ndi abusa omwe tiyenera kuwapewa?

Inde; ambiri a iwo ndi mimbulu yokhala mchikopa cha nkhosa. \_\_\_"Ndipo ndikukudandaulirani, abale, yang'anirani iwo akuchita zopatutsana ndi zophunthwitsa, kosalingana ndi chiphunzitsa cho munachiphunzira inu; ndipo potolokani pa iwo. Pakuti otere satumikira Ambuye wathu Khristu, koma koma mimba yawo; ndipo ndi mau asalaza ndi wosyasyalika asokeretsa mitima ya osalakwa." (Aro 16:17-18)